**EXAMINATION NO.:**___________________________

# CHAMBE ZONE EXAMINATION BOARD

## 2022 STANDARD MOCK EXAMINATION

## CHICHEWA

100 MARKS

**Subject Number:**

**Tuesday, 1st March, 2022**

**Time allowed: 2hrs 15mins**
**(8am – 10:15am)**

**Dzina lanu:**______________________________________________________________________

**Dzina la sukulu yanu:**______________________________________________________________

**Malangizo:**

- Onetsetsani kuti kuti pepala ili lili ndi masamba asanu ndi atatu.
- Lembani dzina lanu ndi la sukulu yanu pa mipata ili mwambayi.
- Lembani nambala yanu ya mayeso pa mpata omwe uli pa pamwamba pa tsamba lililonse.
- Pepala ili lili ndi magawo anayi **A, B, C** ndi **D.**
- Lembani kalata kapena chimangirizo mu gawo **A** ndipo yankhani mafunso onse mu gawo **B**, **C** ndi **D.**
- Chongani mu bokosi lomwe lili ku kutsogolo kwa mafunso omwe mwayankha.
- Pelekani pepala lanu kwa oyang'anira mayeso (invigilator) nthawi yolembera mayeso ikatha.

| Question number | Tick if answered | Do not write anything in these columns | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6 | | | |
| 6 - 10 | | | |
| 11 – 15 | | | |
| 16 – 20 | | | |
| 20 - 25 | | | |
| | | | |

© 2022 CHAZEB

Turn over/…..

**EXAMINATION NO.:___________________________**

**GAWO A: (Malikisi 30)**

Langizo: Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso ali m'musiwa. Sankhani mutu wa chimangirizo kapena wa kalata. Mawu a chimangirizo chanu kapena kalata asachepere 100 koma asabzole 150.

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu "GULE WA KWATHU"

Ndime yoyamba

- Dzina la gule yemwe amavinidwa kwanu
- Anthu omwe amavina guleyu
- Nyengo imene guleyu amavinidwa

Ndime yachiwiri

- Zovala zomwe zimavalidwa povina guleyu
- Zifukwa zovinira guleyu
- Ubwino wa guleyu

Ndime yachitatu

- Momwe mukulimbikitsira guleyu

KAPENA

2. Mwachotsedwa sukulu muli fomu 1 pa Litonga Sekondale Sukulu chifukwa cha makhalidwe anu oipa. Lembani kalata kwa mphunzitsi wamkulu. Litonya Sekondale Sukulu P.O. Bokosi 211 Zomba Yomupempha kuti mubwelerenso.Tsatani izi polemba kalata;

Ndimbe yoyamba

- Tchulani tsiku ndi nthawi yomwe adakuchotsani sukulu
- Fotokozani zifukwa zomwe adakuchotserani

Ndime yachiwiri

- Zovuta zomwe mukukumana nazo chifukwa chokuchotsani sukulu
- Zovuta zatsokoneza bwanji tsogolo lanu?

Ndime yachitatu

- Fotokozani momwe muzikhalira kusonyeza kuti mwasintha mukabwereranso kusukulu.

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

## GAWO B: (Malikisi 20)

KUMVETSA NKHANI

3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kenako yankhani mafunso otsatirawa.

M'mudzi mwa Mbalame mudali nyamata dzina lake Kadyereni.Nyamatayi adali wamtali dzala. Khalidweli adayamba oahkomo la amayi ake a Nadimba ndi a Chigwe. Ngakhale makolo ake amamulangiza kuti khalidweli ndi loipa, Kadyereni zonsezi amazitayira kunkhongo. Atalemba mayeso ake a sitandade 8, Kadyereni adapita ku sukulu yogonera komweko komwe adapitiliza umbava wake pobera anzake mabuku, sopo komanso ndalama.

Poti chozemba chidakumana ndi chokwawa, tsiku lina Kadyereni adagwidwa akuba ndipo ophinzira anzake adakamuneneza kwa mphunzitsi wamkuluyemwe adampatsa chilango cholapitsa kuti asinthe chikhalidwe chake koma iye sadasinthe.

Aphunzitsi adathedwa naye nzeru ndipo adamuchotsa sukulu. Ali kumudzi kwawo Kadyereni sadasiyebe umbava. Iye amaba mnyumba za anthu komanso m'sitolo za mm'udzimo. Tsiku lina adagwidwa apa ndiye anaona zakuda ndipo adakumbukira malangizo omwe makolo adampatsa, poti mawu aakulu akoma akagonera. Apolisi atamva za Kadyereni sadazengereze koma kupita kukamunjata. Mbiri ya kugwidwa komanso kumenyedwa kwa Kadyereni ikudamveka ponseponse ndipo adatsekeredwa m'chitolokosi cha apolisi. Ana onse adadziwa kuti umbava ndi oipa umayikitsa moyo pachiswe.

Tsopano yankhani maunso otsatirawa.

a. Kodi kwawo kwa Kadyereni kudali kuti?
___________________________________________________(1malikisi)

b. Kodi Kadyereni umbava adayambira kuti?
___________________________________________________ (1malikisi)

c. Tchulani zinthu ziwiri zomwe Kadyereni amawabera anzake kusukulu.
___________________________________________________ (2malikisi)

d. Pezani mkuluwiko ofanana m'matanthauzo ndi uwu "onyalanyaza"
___________________________________________________ (1malikisi)

e. Fotokozani zomwe mphunzitsi wamkulu adamuchitira Kadyereni.
___________________________________________________
___________________________________________________ (2malikisi)

f. N'chifukwa chiyani Kadyereni adamuonetsa zakuda?
___________________________________________________
___________________________________________________ (2malikisi)

g. Mukuganiza kuti chifukwa chiyani a polisi sadachedwe kukamunjata Kadyereni?
___________________________________________________
___________________________________________________(2malikisi)

h. Pezani matanthauzo a mikuluwiko iyi:
i) kuthedwa nzeru
___________________________________________________ (1malikisi)

ii) chozemba chinakumana ndi chokwawa
_________________________________________________ (1malikisi)

i. Perekani phunziro lomwe mwapeza m'nkhaniyi
_________________________________________________________
_________________________________________________ (1malikisi)

j. Perekani mawu osutsana m'matanthauzo ndi awa:
i) kumbukira ________________________________________ (1malikisi)
ii) mangidwa________________________________________ (1malikisi)

k. Perekani mutu wa nkhaniyi
_________________________________________________ (2malikisi)

**GAWO C: (Malikisi 10)**

4a. Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawoa

"Chaka chino ndaganiza mozama. Ndikufuna kuti tonse tibzale mbewu ya makono yachimanga kuti m'mudzi muno musadzadutsenso galu wakuda."

Mafunso

i) Ndi malonje anji amenewa?
_________________________________________________ (1malikisi)

ii) Kodi malonjewa akuyankhulidwa kwa yani?
_________________________________________________(1malikisi)

iii) Mawu oti "galu wakuda" akutanthauzanji?
_________________________________________________ (1malikisi)

b. Kodi pamsewu nyali yachikasu imatanthauzanji?
_________________________________________________ (1malikisi)

c. Perekani njira imodzi yotumizira uthenga wa ukwati.
_________________________________________________ (1malikisi)

5. Kupanga ziganizo.
Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:

a. tchona
_________________________________________________ (1malikisi)

b. thimbwizika
_________________________________________________ (1malikisi)

c. mbee
_________________________________________________(1malikisi)

d. mbutuma
_________________________________________________(1malikisi)

e. chitete
_________________________________________________(1malikisi)

**EXAMINATION NO.:**___________________________

## GAWO D

Zungulitsani lembo lokhonza **(A,B, C Kapena D)** m'mafunso otsatirawa.

Mafunso 6 mpaka 10: Sankhani mitundu a mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo.

6. Mkango <u>ndi</u> chilombo choopsa.
   A. Mlumikizi C. Mperekezi
   B. Mvekero D. Mneni

7. <u>Moyo</u> umenewu siwabwino.
   A. Dzina C. Mvekero
   B. Mneni D. Mfuwu

8. <u>Imodzi</u> apezeka m'nyumba ya a Bwande.
   A. Mfotokozi C. Dzina
   B. Mlowam'malo D. Muonjezi

9. Amayi amandikaniza kupita <u>kutali</u>.
   A. Mfotokozi C. Mperekezi
   B. Dzina D. Muonjezi

10. Achule amakhala <u>m'madzi</u>
    A. Dzina C. Muonjezi
    B. Mperekezi D.Mlumikizi

Mafunso 11 mpaka 15: Sankhani mutundu ya nthawi za aneni yomwe yatsekedwa mzere kunsi kwawo.

11. Amisiri <u>akumanga</u> nyumba.
    A. yatsopano yathayi
    B. yatsopano
    C. yatsopano yopitilira
    D. yatsopano yakawirikawiri

12. Belita <u>anali ataweruka</u> pamene amchita ndewu
    A. yatsopano yopitilira
    B. yakale opitilira
    C. yakale yathayi
    D. yatsopano yathayi

13. Chimango <u>abagulitsa</u> chinangwa.
    A. yatsopano
    B. yamtsogolo
    C. yakale
    D. yamtsogolo yopilira

14. Atsikana <u>akuvina</u> chioda.
    A. yamtsogolo yopitilira
    B. yatsopano yopitilira
    C. yamtsogolo yathayi
    D. yatsopano yathayi yopitilira.

15. Iwo <u>amalima</u> mpunga.
    A. Yatsopano akawirikawiri
    B. yamtsogolo
    C. yakale
    D. yatsopano yathayi yopilira

Mafunso 16 mpaka 18: Sankhani mawu otsutsana m'matanthauzo ndi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo.

16. Banja ilo lili <u>pa chisoni.</u>
    A. Pa chikondi C. Pa mtendere
    B. Pa ufulu D. Pa chimwemwe

17. Ife ndife <u>nzika</u> za M'malawi.
    A. mfulu C. mlendo
    B.kapolo D. mkamwini

18. <u>Umphawi</u> wafika povuta kwambiri.
    A. Utchisi C. Ukapolo
    B. Ulemelero D. Umbanda

19. Iwo mapita ku sukulu kuti akaphunzire kulemba.
    A. yoima payokha
    B. yadzina
    C. yamfotokozi
    D. yamuonjezi

20. Ng'ombe yomwe waphayi ndi yanga.
    A. yadzina D. yoyima payokha
    B. yamfotokozi C. yadzina

21. Zomwe mwapatsidwazo ndi zofunika kwambiri.
    A. yadzina C. yamuonjezi
    B. yamfotokozi D. yoima payokha

Mafunso 22 mpaka 26: Sankhani matanthauzo a mikuluwiko yotsatirayi.

22. Suzumire adaphetsa mkhalakale.
    A. Sibwino kuchita zinthu mwachangu
    B. Anthu okalamba amafa mwadzidzidzi.
    C. Kusaugwira mtima kumadzetsa mavuto.
    D. Kusasamala kumaonongetsa zinthu.

23. Chifundo chidaphetsa Msema mitondo.
    A. Sibwino kukhala ndi luso lapadera
    B. Chifundo chimaiwalika pa mavuto
    C. Ntchito iliyonse ili ndi mavuto ake.
    D. Chifundo nthawi zina chimapweteketsa.

24. Nkhondo ndi anansi.
    A. Abale amatikonda pamtendee pokha.
    B. Abale nthawi zina amafunirana zoipa.
    C. Abale nthawi zina sayamika.
    D. Abale saoneka pa mavuto.

25. Taya udzu omwetamweta.
    A. Kusachitapo kanthu mavuto ukawaona.
    B. Kusadziwa chochita pa mavuto.
    C. Kusagwiritsa ntchito mwayi opezapeza.
    D.Kusazindikira kuti uli ndi nzeru za padera.

26. Ndionetsetse adathetsa nkhosa.
    A. Kuzengereza kumapezetsa mavuto.
    B. Changu chimapezetsa mavuto.
    C. Ukaona zinthu uziuza anzako.
    D. Tizionetsetа zinthu tisanachitepo kanthu.

Mafunso 27 mpaka 30: Sankhani magulu a mayina omwe ali ndi mzere kunsi kwawo.

27. Wanyamula <u>katoni</u> ya sopo.
    A. Mu-, Mi-  C. Li-, Ma-
    B. Ka-, ti-  D. Mu-, A-

28. Ng'ombe zathawira <u>m'tchire</u>.
    A. Ku-, Pa-, Mu-
    B. Ku- ndi tsinde la Mneni
    C. Mu-, Mi-
    D. Chi-, zi-

29. Atate amadana ndi <u>mwambo</u> wa chinamwali.
    A. I-, Zi-  C. Mu-, Mi-,
    B. Li-, Ma-  D. U-, Ma-

30. Mafuli adandibera <u>uchi</u> wanga.
    A. Chi-, Zi-  C. Mu-, Mi-
    B. Mu-, A-  D. U-, Ma-

Mafunso 31 mpaka 35: Sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro za m'kalembedwe zoyenera.

31. A. Kodi mnkhaniyi mwaphunziramo chiyani?
    B. Kodi m'nkhaniyi mwaphunziramo chiyani?
    C. Kodi mn'khaniyi mwaphunziramo chiyani?
    D. Kodi m'nkhaniyi mwaphunziramo, chiyani?

32. A. Mnyamata iwe penyetsetsa kuti uwone zenizeni.
    B. Mnyamata iwe! Penyetsetsa kuti uwone zenizeni.
    C. Mnyamata iwe, Penyetsetsa kuti uwone zenizeni.
    D. Mnyamata iwe. Penyetsetsa kuti uwone zenizeni.

33. A. Ndi liti? Duwa lomwe silinapsonthedwe.
B. Ndi liti duwa lomwe silinapsonthedwe?
C. Ndi liti! Duwa lomwe? silinapsonthedwe
D. Ndi liti duwa lomwe silinapsonthedwe!

34. A. Mbale zili mbwe! pabwalo.
B. Mbale zili mbwe, pabwalo.
C. Mbale zili mbwe pabwalo.
D. Mbale, zili mbwe pabwalo.

35. A. Chifukwa cha njala iye adamwa zakumwa zone.
B. Chifukwa cha njala iye, adamwa zakumwa zone.
C. Chifukwa cha njala iye adamwa, zakumwa zone.
D. Chifukwa cha njala, iye adamwa zakumwa zone.

Mafunso 36 mpaka 40: Sankhani msintho wa aneni omwe atsekedwa mzere kunsi kwa ziganizo zotsatirazi.

36. Anawa <u>adaleledwa</u> bwino.
A. Wochitidwa C. Wochitirana
B. Wochititsa D.Wochititsitsa

37. Osewera onse <u>amavala</u> Malaya ofanana.
A. Wochititsa C.Wobwerezabwereza
B. Otsutsa D. Wochitidwa

38. Anthu ena <u>amatolatola</u> zinthu za eni.
A. Wobwerezabweraza
B. Wochitira
C. Wochitirana
D. Onyazitsa

39. <u>Penyetsetsa</u> kuti uwone zenizeni.
A. Wochititsa C. Wochititsitsa
B. Wochitidwa D. Owonetsetsa

40. Atsikanawo <u>amenyerana</u> mwamuna.
A. Wochititsa
B. Wochitidwa
C. Wobwerezabwera
D. Wochitirana

Mafunso 41 mpaka 45: Sankhani matanthauzo oyenera a zilapi izi.

41. Mfuti yanga yoalsira kumbuyo
A. tombolombo C. ntchentche
B. njuchi D. nthonga

42. Mbalame yoikira paminga.
A. mutu C. lilime
B. mano D. maso

43. Muvi wa atate chiboola tsindwi
A. utsi C. lilime
B. mpaliro D. mano

44. Nyama pamwamba, chikumba mkati.
A. chiwindi C. chikhadabo.
B. chivututu D. mango

45. Amayi tsalani kunyumba ndipita ndi ine.
A. chimanga C. mapesi
B. masamba D. mwana

**MAFUNSO ATHERA PANO**